



MZIMBA NORTH EDUCATION MANAGEMENT

2026 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION CHICHEWA

(100 Malikisi)

Thursday, 19th March

Subject Number: P032
Time allowed: 2hr 15 mins
1:00 - 3:15pm

Dzina lanu: _____

Dzina la Sukulu yanu: _____

Malangizo

- Onetsetsani kuti pepalali liri ndi masamba otsindikizidwa khumi.
- Pepala ili liri ndi magawo anayi: **Gawo A, B, C** ndi **D**
- Lembani **dzina la sukulu** yanu pamwamba pa tsamba lino.
- Lembani nambala ya mayeso pamwamba pa tsamba lililonse.
- Lembani chimangirizo kapena kalata mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi **D**.
- Muchitebulo chiri pambalichi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.

- Perekani kwa okuyang'anirani kulemba mayeso (**imvigireta**) pepala lonseli nthawi ikakwana.

Funso	Chongani zomwe mwayankha	Muno musalembemo	
1			
2			
3			
4			
5			
6-45			

Yankhani funso **limodzi lokha** mwa mafunso awiri ali m'musimu. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo kapena kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu: “**MUDZI WAKWATHU**”. Mwa zina tsatani izi polemba chimangirizo chanu.

Ndime yoyamba

- Tchulani dzina la mudzi wanu
- Tchulani chigawo chomwe mudziwu ukupezeka

Ndime yachiwiri

- Fotokozani mitundu ya anthu ndi ziyankhulo zawo
- Fotokozani magule amene anthu a m'mudziwu amakonda kuvina
- Longosolani njira zomwe anthu am'mudziwu amapezera chuma

Ndime yachitatu

- Fotokozani mavuto omwe anthu am'mudziwu amakumana nawo
- Fotokozani momwe mavutowo angathetsedwere

KAPENA

2. Lembani kalata kwa m'bale wanu yemwe akukhala kutali ndi inu yomufotokozera kuti mumadwala koma tsopano mwachira.. Mwa zina tsatani izi polemba kalata yanu:

Ndime yoyamba

- Matenda omwe mumadwala
- Nthawi yomwe matendawo adayamba
- Nthawi yomwe mudachira

Ndime yachiwiri

- Momwe matendawo adayambira
- Chomwe mudachita mutadwala
- Momwe mudathandizidwira kuti muchire

Ndime yachitatu

- Zomwe mukuchita kuti musadwalenso matendawo

[illegible]

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.

M’dera la Masogona mudali mudzi wotchedwa Bwatani. Derail lidali la mkaka ndi uchi. Kum’awa kwa derali kudali nyanja yaikulu komanso yokongola. M’nyanjayi mudali nsomba zosiyanasiyana monga: Chambo, mphuta, micheni, milamba ndi zina zambiri.

Anthu a m’derali adali ogwirizana kwambiri motero chitukuko chidali ponseponse monga: mijigo, sukulu, zipatala, milatho ndi nyumba za makono. Chifukwa cha chidwi chomwe anthu amaonetsa, mabungwe ambiri amalithandiza derali ndi mphatso zosiyanasiyana. Anthu ambiri adali a thanzi ndi anyonga chifukwa amapeza zofuna zawo mosavutika. Nkhani ya umbava ndi Umbanda kwa iwo idali nkhamba kamwa chifukwa padalibe uyo adali pamavuto oti angayambitse mchitidwe woyipawu.

M’mudzi wina kuvuma kwa derali mudali nyakwawa yotchedwa Nguli. Nyakwawayi idali yokonda madyeramphotho. Chifukwa cha khalidwe loyipali, nyakwawa Nguli idali zayakunkhongo. Iyo simalabadira kumva zomwe imalangizidwa ndi nduna zake. Nduna zake Ngolingo ndi Khomani, adayetsetsa kuidzudzula koma idakanika.

Tsiku lina bungwe lomwe si la boma lidapereka ziphaso zolandilira chakudya chaulele, chifukwa madzi otsefukira adaononga katundu ndi mbewu m’mudzimbu. Nyakwawa Nguli idagawira anthu ochepa ndipo zambiri idagulitsa kwa khumutcha wina wotchedwa Ngondoma. Akazi anyakwawa Nguli a Nambewe adatumbwa chifukwa cha ndalama zomwe amuna awo adali nazo.

Anthu atamva kuti nyakwawa Nguli idagulitsa ziphatso zina, iwo adapita kukamang’ala kupolisi. Ndipo apolisi adapita kukathira unyolo nyakwawa Nguli. Ataipanikiza ndi mafunso, iyo idaulula kuti idagulitsa ziphaso zina kwa khumutcha ndipo naveso adamunjata. Tsiku la mlandu litafika, nyakwawa ndi khumutcha uja adapezeka olakwa. Adawalamula kupita kundende ndi kukagwira ntchito ya kalavula gaga kwa zilumika zisanu.

Anthu a m’mudzi muja adasankha nyakwawa ina. Nyakwawa yatsopanoyo idakhazikitsa magulu oti aziphunzitsa anthu nkhani zokhuza katangale. **(buku la ophunzira la sitandade 6)**

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

a) Kodi mudzi wa Bwatani udali m’dera liti?

_____ **(malikisi 1)**

- b) Tchulani zitukuko ziwiri zokha zomwe zidabwera m'derali
 _____ (malikisi 2)
- c) N'chifukwa chiyani mabungwe amathandiza derali?
 _____ (malikisi 2)
- d) N'chifukwa chiyani anthu a derali adali a thanzi ndi anyonga?
 _____ (malikisi 1)
- e) Perekani makhalidwe awiri a nyakwawa Nguli.
 _____ (malikisi 2)
- f) Pezani mawu m'nkhaniyi omwe matanthauzo ake ndi awa:
 i. Munthu osamva za anthu ena
 _____ (malikisi 1)
 ii. Dandaula mlandu
 _____ (malikisi 1)
- g) Perekani mayina awiri a nduna za nyakwawa Nguli.
 _____ (malikisi 2)
- h) Anthu adadziwa bwanji kuti nyakwawa Nguli yagulitsa ziphatso?
 _____ (malikisi 1)
- i) Kodi anthu a m'mudzimu adachita chiyani pokwiya ndi khalidwe la nyakwawa Nguli?
 _____ (malikisi 1)
- j) Lembani tathandizo la chining'a ichi
 Mkaka ndi uchi
 _____ (malikisi 2)
- k) Fotokozani chifukwa chimene a Nguli ndi a Ngondoma adanong'onezera bondo
 _____ (malikisi 2)
- l) Perekani ubwino umodzi osachita katangale m'dziko
 _____ (malikisi 1)
- m) Perekani mutu oyenera wa nkhaniyi
 _____ (malikisi 1)

GAWO C: (Malikisi 10)

Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli.

Malonje

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawa.

“Paja wathuyu amati waona kodyakokha kuno ndiye tati aaa, tiyeni tilondole kuti tikamvetse paja zakumva ziwawa m’makutu.”

Mafunso

- i. Tchulani mtundu wa malonjewa _____ (malikisi 1)
 - ii. Angalankhule mawuwa ndi ndani? _____ (malikisi 1)
 - iii. Kodi malonjewa akuchitikira kuti? _____ (malikisi 1)
 - iv. Mawu oti kodyakokha akutanthauzanji? _____ (malikisi 1)
 - v. Tchulani njira imodzi yomwe anthu angafalitsire uthenga wa Mulungu. _____ (malikisi 1)
5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa: (malikisi 5)
- i. mpingo _____
 - ii. nkhawena _____
 - iii. zingalume _____
 - iv. khwimbi _____
 - v. moipa _____

GAWO D: (40 Malikisi)

Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C kapena D) m’mafunso itsatirawa.

- Mafunso 6 mpaka 10:** Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kungsi kwawo.
6. Kodi simukufuna?
 A. Mneni C. Muonjezi
 B. Mlowam’malo D. Mfotokozi
7. Anthu aja athambitsidwa zedi.
 A. Muonjezi C. Mfotokozi

- B. Mlumikizi D. Mneni
8. Awabera katundu wawo dzulo.
 A. Mfotokozi C. Dzina
 B. Mlowam’malo D. Mvekero
9. Inu muzithokoza Mulungu
 A. Muonjezi C. Mneni
 B. Mlowam’malo D. Dzina
10. Jonasi adagwa pansi kuti khu.

2026

A. Mperekezi

C. Mfuwu

B. Muonjezi

D. Mvekero

Mafunso 11 mpaka 15: Sankhani

matanthauzo a mawu omwe ali ndi mzere
kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

11. Kuyenda utsi uli tsitu.

A. Kusinza

C. Kuyenda mofatsa

B. Kupusa

D. Kuyenda utatsinzina

12. Iye uja ndi pakomaine.

A. Munthu wodanitsa

B. Munthu wochita zoti amakonda

C. Munthu wamisala

D. Munthu waulemu

13. Ndipsi amasokoneza dziko.

A. Wauve

C. Waulesi

B. Wamwano

D. Wakuda

14. Tata anashomola nkhandwe.

A. Analalata

C. Analangidwa

B. Anapalamula

D. Anamenyedwa

15. Mayi ake adabzala chinangwa.

A. Adapita kumanda

B. Adadwala

C. Adakalima

D. Adamwalira

Mafunso 16 mpaka 20: Sankhani nthambi

ya ziganizo zosaima pazokha zomwe
zatsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo
zotsatirazi.

16. Zoti Nyanja yanthu ikuphwa ndizoona.

A. Ya muonjezi

B. Yoyima payokha

C. Ya mfotokozi

D. Ya dzina

17. Namwino uja adafotokoza monga
ankadziwira.

A. Ya dzina

B. Ya mfotokozi

C. Yoyima payokha

D. Yamuonjezi

18. Iyi ndi nthawi yomwe timabzala
mitengo.

A. Yoima payokha

B. Ya dzina

C. Yamuonjezi

D. Yamfotokozi

19. Iwo andiona pomwe ndimatuluka
mn'yumba.

A. Yamfotokozi

B. Ya dzina

C. Yoyima payokha

D. Yamuonjezi

20. Udzapambana mayeso pokhapokha
ukadzalimbikira.

A. Ya muonjezi

B. Yoyima payokha

C. Ya mfotokozi

D. Ya dzina

Mafunso 21 mpaka 25: Sankhani

chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro za
m'kalembedwe zoyenera m'ziganizo
zotsatirazi

21.

A. Ha? Mwanawe, andithangate ndani?

B. Ha! Mwanawe andithangate ndani?

C. Ha! Mwanawe, andithangate ndani?

D. Ha, Mwanawe, andithangate ndani?

22.

A. Kodi ukulemba, chiyani Nyanyiwe?

B. Kodi ukulemba chiyani, Nyanyiwe?

C. Kodi, ukulemba chiyani Nyanyiwe?

D. Kodi ukulemba chiyani? Nyanyiwe

23.

A. "Bweretsa bukulo adatero,"

Aphunzitsi

B. "Bweretsa bukulo adatero,"

Aphunzitsi

2026

- C. “Bweretsa bukulo,” adatero
aphunzitsi
- D. “Bweretsa bukulo, adatero”
aphunzitsi

24.

- A. Aphunzitsi anena kuti tisingolole.
- B. Aphunzitsi anena, kuti tisingolole.
- C. “Aphunzitsi anena” kuti
tisingolole.
- D. “aphunzitsi anena kuti tisingolole.”

25.

- A. nchifukwa chiyani mumandinyoza?
- B. “Nchifukwa chiyani mumandinyoza?”
- C. N’chifukwa chiyani mumandinyoza?
- D. n’chifukwa chiyani mumandinyoza?

Mafunso 26 mpaka 30: Sankhani misintho
ya aneni omwe atsekedwa mzere kungsi
kwawo m’ziganizo zotsatirazi

26. Kapu yanga idasweka.

- A. Wom’chitira
- B. Wochitirana
- C. Wochititsa
- D. Wochitidwa

27. Agogo awaphikira chakudya.

- A. Wochititsa
- B. Wom’chitira
- C. Wochitirana
- D. Wochitidwa

28. Njinga zija zaombana.

- A. Wochititsitsa
- B. Wochitidwa
- C. Wochitirana
- D. Wochititsa

29. Awa amagonagona

- A. Wochititsitsa
- B. Wobwerezabwereza
- C. Wotsutsa
- D. Wochitidwa

30. Iye wamasula thumba lija.

- A. Wom’chitira
- B. Wochititsa
- C. Wotsutsa
- D. Wochitidwa

Mafunso 31 mpaka 35: Sankhani mitundu
ya afotokozi omwe ali ndi mzere kungsi
kwawo m’ziganizo zotsatirazi.

31. Undibwereke buku lililonse.

- A. Woloza
- B. Wopatula
- C. Wa umwini
- D. Wa mgwirizano

32. Iye wavala Malaya otuwa.

- A. Wa makhalidwe
- B. Wa umwini
- C. Woloza
- D. Wa maonekedwe

33. Wagula mbuzi zinayi.

- A. Wa maonekedwe
- B. Woloza
- C. Wa mawerengero
- D. Wa makhalidwe

34. Galu wolusa uja waphedwa.

- A. Wopatula
- B. Wa maonekedwe
- C. Wa makhalidwe
- D. Woloza

35. Zinthu zomwe amafuna wazipeza.

- A. Wa umwini
- B. Wa mgwirizano
- C. Wa maonekedwe
- D. Woloza

Mafunso 36 mpaka 40: Sankhani
matanthauzo oyenera a ndagi zotsatirazi.

36. Kankhalamba aka kusambasamba

- A. Chule
- B. Chiponde
- C. Nthiko
- D. Fulu

37. Ndikati tsogolo iye amakana

- A. Mwana C. Phazi
B. Chidendene D. Zala

38. Kungatalike lero lomwe nkafika

- A. Maganizo C. Kumwamba
B. Kutawuni D. Ku munda

39. Chitsime cha agogo kusaphwa

- A. Kasupe C. Mkamwa
B. Nyanja D. Mjigo

40. Nyumba za m'phiri zopanda zitseko.

- A. Mphuno C. Makutu
B. Maso D. Mawondo

Mafunso 41 mpaka 45: Sankhani ntchito za “ndi” m'ziganizo zotsatirazi.

41. Ndidzapita ku sukulu sabata ya mawa.

- A. Mlumikizi
B. Mlowam'malo
C. Mperekezi
D. Mneni

42. Chakudyacho chikhale cha ndi.

A. Mperekezi

B. Mvekero

C. Mlowam'malo

D. Mneni

43. Ophunzira ali ndi aphunzitsi awo.

A. Mperekezi

B. Mlowam'malo

C. Mlumikizi

D. Mneni

44. Mulungu amatikonda ndi kutisamala.

A. Mneni

B. Mlumikizi

C. Mperekezi

D. Mvekero

45. Anyamata ndi ochenjera kwambiri.

A. Mperekezi

B. Mlumikizi

C. Mneni

D. Mlowam'malo

MAFUNSO ATHERA PANO

NB: Pepala ili liri ndi masamba otsindikidzidwa khumi